

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

MCHIRITSI WAMKULU

(Nkhani yotsatirayi ikutengedwa pa zimene zinachitika pa Marko 5:24-34).

Anthu anaunjikana pamene Yesu amayenda mu mseu wa fumbi. Ophunzira ake anamuzungulira Yesu ndipo amafuna kuti amutchinjirize ku chikhamu cha anthucho chimene chinali kupanikizabe ndi kuyandikira. Pamamveka kuseka pamene ana amathamangathamanga pakati pa anthuwo. Kumamvekanso mau a abambo ndi amai amene amakambirana ndi kuuzana zimene anazona. Panali chiphokoso chokhachokha. Munthu wina wolumala, pokanika kuyenda bwinobwino anaterereka ndi kugwa gululo nkumapita. Mai wina, atanyamula mwana wodwala malungo, anafika pa khamulo akuthamanga nafunitsitsa kuti akakumane ndi Ambuye.

Mkatikati mwa chikhamu cha anthucho munali mai wina, amene anayesetsa kudzikankha ndi cholinga choti akafike pamene panali Yesu. Iye anafunda nsalu kumaso ndipo anali wonyololoka ndi wotumbuluka, maso ake omwe anali atalowa mkati komabe anali kutsatira pambuyo pa Yesu ndipo moofoka momwemo anayesetsa kudzikankha kuti akafike pamene panali Yesu. Maiyo anali akudwala kwambiri ndipo anakhala akutaya mwazi kwa zaka 12. Iye anavutika kwambiri ndipo anapita kwa asing'anga ndi azachipatala osiyanasiyana koma osathandizika. Anaononga chuma chake chonse kufunafuna machiritso, koma m'malo mwake zinthu zimanka ziipiraipira popeza panalibe munthu amene akanatha kumuchiritsa.

Tsiku lina anamva za munthu wotchedwa Yesu. Iye anamva zakuti Yesuyo amayenda mudzi ndi mudzi kuchiritsa matenda ndi kudwala kosiyanasiyana. Iye anamva zakuti amatulutsa


mizimu yoipa, kupangitsa kuti olumala ayende komanso akhungu kuti apenye. Iye anaganiza mu mtima mwake nati, "Zoonadi Yesuyu, amene ali mphunzitsi ndiponso munthu wa Mulungu, akhoza kundichiritsa ine."

Mokhulupirira ndi moyembekezera, iye anapita kukafunafuna Yesu. Ndipo anamupeza, koma anali wotanganidwa komanso pakati pa chipiringu cha anthu. Iye anaganiza nati mkati mwake, "Ngati ndikakhudza ngakhale zovala zake ndidzapulumutsidwa." Ndi chikhulupiriro chimenechi, anayamba kudzikankhiza mkati mwa khamulo. Pamene anaona kuti wayandikira, anatansa dzanja lake nakhudza ophunzira kenaka anakhudza chovala cha Yesu. Thupi lake linayamba kutentha ndipo nthawi yomweyo thupi lake linachiritsidwa ndipo analandira mphamvu ndi moyo watsopano.

Pamene maiyo anaima akudabwa ndi kuyamika Mulungu chifukwa zimene zinamuchitikirazo, Yesu naye anaima natembenuka ndi kufunsa, "Ndani anakhudza zovala zanga?" Ophunzirawo anamuyankha kuti, "Muona kuti khamu lilikukanikiza Inu, ndipo munena kodi, Wandikhudza ndani?" Yesu anapitiriza kuyang'anayang'ana, popeza anamva ndithu kuti mphamvu ina ya machiritso yatuluka m'thupi mwake.

Maiyo, tsopano akunjijemera, anagwa pamapazi a Yesu namuza za kudwala kwake komanso za m'mene anachiritsidwira nthawi yomweyo. Mwa chikondi komanso mwachifundo, Yesu anati, "Mwana wamkaziwe, chikhulupiriro chako chakupulumutsa; muka mumtendere, nukhale wochira chivutiko chako."

(Yapitirira pa tsamba 2)



"Ngati ndikakhudza ngakhale zovala zake ndidzapulumutsidwa."

Mau a Mkonzi

3

Kusanthula Baibulo: Chiphunzitso cha machiritso akumwamba

4

Nkhani Yotsagana Nayo: Machiritso akumwamba

5

Mafunso ndi Mayankho

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

M'mene Yesu Khristu amachitira zinthu zake zinali zodabwitsa ndi zododometsa. Pamene anali panso pano, Yesu anachita zodabwitsa zambiri pamene anthu anamukhulupirira ndi kumudalira Iye. Anthu amene anabwera kwa Iye sanabwerere kwao chimodzimodzi. Yesu anatumikira osati ku uzimu wokha komanso ku zosowa za anthu za kuthupi. Yesu anamuchitira mai uja zimene anthu ophunzira anakanika kumuchitira—Iye anachiritsa thupi lake ndi mphamvu yakumwamba ndipo amamuchiritsa modabwitsa. Yesu analidi mchiritsi wamkulu panthawiyo ndipo tikuyamika Mulungu kuti ngakhale lero akadali mchiritsi wamkulu.

Pakadali mphamvu ndi ubwino mu machiritso a mwa Yesu Khristu. Yesu akupitirizabe kutumikira kwa iwo amene abwera kwa iye mwa chikhulupiriro, iwo amene ali odwala ndi osweka. Yesu akadali pa ntchito yopulumutsa moyo uwo umene uli omangika mu uchimo, komabe iye amakondweretsedwa kutumikira anthu amene akusautsika m'moyo wao ndi nyengo zopweteka ndi zowawa. Yesu sakulowa m'malo mwa madokotala kapena ena onse azachipatala. Iyeyo ndi Mulungu woona ndi wamphamvu amene akhoza kuchita mopambana ndi moperera pa zimene munthu akhoza kukwaniritsa. Palibe chosatheka ndi Mulungu. Pamene chiyembekezo chapita ndipo palibe mayankho, kuwala ndi chisomo cha machiritso akumwamba kuchokera kwa Yesu chikhoza kulowa mu mdima ndi kusinthiratu modabwitsa nkhwana ndi kupweteka kwa m'thupi zimene zimabwera chifukwa cha kudwalako.

Mai amene anachiritsidwa anataya nthawi, mphamvu ndi ndalama zake kufunafuna machiritso pa chifukwa cha kudwala kwake. Ife lero tili ndi mwai wakuti tikudziwa za Yesu ndipo sitiyenera kuchedwa kapena kuzengereza. Tikhoza kubwera ndi mavuto komanso zosowa zathu kwa Iye nthawi ina iliyonse ndipo Iye akudikira mwachikondi kuti atichitire ife zimene sitingathe kuchita patokha. ■



Mu maweruzidwe a mpingo, pali nthawi zina pamene anthu amaoneka kuti sakufikapo pa kukhulupirira Mulungu pa nkhani zokhudza matenda akuthupi. Kodi anthu oterewa tiwalandire motani?

“Ndipo iye amene ali wofooka m'chikhulupiriro, mumlandire, koma si kuchita naye makani otsutsana ai” (Aroma 14:1). Pokhala oyera mtima, tikhale okonzeka kuwagwiriziza abale ndi alongo athu m'pemphero ndi kuwakonda osati kuwadzudzula.

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvumere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



[Mulungu] ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhazikitsa pamodzi m'zakumwamba mwa Khristu Yesu; kuti akaonetsere m'nthawi zilinkudza chuma choposa cha chisomo chake, m'kukoma mtima kwa pa ife mwa Khristu Yesu. —Aefeso 2:6-7

Zisomo za Ambuye Yesu Khristu zikuyendererabe kwa ife ngakhale mu nthawi yathu ino. Ndi mdalitso waukulu kukhala nao olandira chikondi ndi kukoma mtima kuchokera kwa Mpulumutsi. Mutu wathu ulendo uno ndi wa machiritso akumwamba. Mutu umenewu, wakhala gwero la mtsutso kwa anthu ambiri kuyambira kale ndithu makamaka m'mene tingaugwiritsire ntchito pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Cholinga cha kalatayi ndicho kulimbikitsa chiphunzitsa cha m'Baibulo, posawerengera zimene zaphunzitsidwa mibadwo yapita komanso kamvetsedwe kake. Ngakhale mu mpingo wa Church of God, pakhala pali kukula ndi kusefukira kwa kamvetsedwe ndi machitidwe osiyanasiyana pakati pa atumiki a Mulungu mu mibadwo yosiyanasiyana. Chimenechi ndiye chifukwa chake kuti kofunikira kwa ife kuti tilalikire Mau ndiponso kuzindikira kuti Mzimu awapatsa moyo komanso kutitsogolera m'njira imene Mulungu angakonde kuti ife tikhaliwe.

Pali chisomo cha machiritso athupi chimene mpaka lero chikuyendererabe kuchokera ku mpando wachifumu wa Mulungu. Ineyo ngati munthu ndikhoza kuchitira umboni kuti ndapeza moyo wa chikhulupiriro kukhala wopindulitsa ndi wonditonhoza pamene ndakumana ndi anamondwe a moyo uno. Oyera mtima alero akhoza kunena nkhani zochuluka za kulowererapo kwa machiritso odabwitsa ochokera kwa Mulungu pa nthawi imene panali kudwala komanso matenda. Popanda thandizo lakuchipatala, Mulungu mwamphamvu yake anandibweza ine kuchokera ku dzenje la manda. Iye anandichiritsa ine ku matenda komanso ku kudwala kosiyanasiyana. Achipatala ankanena kuti sindidzayendanso kapena kugwiritsa ntchito manja anga, koma nditasauka kwa zaka zochuluka, Ambuye anachita chinthu chodabwitsa pathupi langa. Ilipo nthawi imene ndakhala pansu pa mphamvu ya Mzimu Woyera pamene ziwanda zimatulutsidwa ndipo anthu nachiritsidwa. Mulungu wakhala akuchiritsa modabwitsa matupi a ana anga ndipo wachita zambiri zimene sindingakwanitse kuzilemba m'kalatayi chifukwa cha kuchepa kwa malo. Machiritso akumwamba si chinthu chimene chinachitika kale basi—ndi zoonadi, ndipo mpaka lero zikuchitikabe.

Chofunika kwambiri ndicho kudalira pa Mulungu kuti ngakhale pachitike zotani, chikhulupiriro chathu chikhale chozikika pa Iyeyo. Ndakhala ndikuona komanso zandichitikirapo kangapo konse kuti panthawi imene ndinali kusautsika komanso pamene Mulungu amaoneka ngati sakundiyankha. Mu nyengo zimenezo, ndikhoza kuchitira umboni kuti ndaona Mulungu akugwira ntchito mu njira zimene sindingathe kuzinena chifukwa zinaposa zomwe ndimaganizira. Kodi sitingadalire nzeru zake monganso m'mene timadalira mphamvu yake ya machiritso?

Tikukhala mu mbadwo umene sufuna kukumana ndi mavuto komanso sufuna kudikira. Pofuna kuti titumikire Mulungu mwachikhulupiriro, tikufunika kuti mkati mwathu mukhale mtendere umene ungapangitse kuti tigonjere ku chifuniro ndi cholinga cha Mulungu. Mzimu wa Mulungu adzakhala wokhulupirika kutsogolera wina aliyense wa ife payekhapayekha mu choonadi. Zimatengera kukhala ozama pa moyo wathu wauzimu kuti tikavomereze kuti Mzimu Woyera akhoza kugwira ntchito mwa ife payekhapayekha, ngakhale kuti nthawi ndi nthawi pakhoza kukhala kusiyana pa zinthu zina zing'onozing'ono.

Sindingathe kulemba mndandanda wa zoyenera kuzichita kapena kusachita zokhudzana ndi nkhani zimene tikukambiranazi, popeza ndikatero penapake ndikhoza kukodwa ndi kudzitsutsa ndekha, komanso mwina kungopereka maganizo a anthu, kapenanso kuchita mwapawiripawiri monga m'mene ena akhala akuchitira m'mbuyomu. Choonadi chake ndi ichi chakuti tili ndi mwai wokhulupirira kwathunthu mwa Ambuye ndipo chimenechi si goli lozunza, koma ndi nthawi younikanso malemba komanso ubale wathu ndi Mulungu.

Ndikukupemphani kuti muike chikhulupiriro chanu mwa Ambuye ndiponso kufunafuna chifuniro chake chakumwamba pa gawo limeneli la moyo. Sitingapemphenso wina wabwino koposa amene ali Mpulumutsi, m'bale, wopereka komanso dokotala. Zoonadi, iye akuyenera kuti timukhulupirire.

Michael Smith
April 2018



Mukafuna kutipeza
pa intaneti, mulembe
www.thegospeltruth.org
kuti mudzilandira makalata
athu kapenanso kuti
muone makalata akale.

Kalozera posanthula Mau a Mulungu

Mutu: Chiphunzitso cha machiritso akumwamba

Kuwerenga Malemba: Zoonadi Iye anyanyamula zowawa zathu, ndi kusenza zisoni zathu; koma ife tinamuyesa wokhomedwa, wokanthidwa ndi Mulungu, ndi wovutidwa. Koma Iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natundudzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango chotitengera ife mtendere chinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yake ife tachiritsidwa. — Yesaya 53:4-5

Mwachidule: Gawo limodzi la cholinga cha Khristu ndiko kutumikira ku zosowa za anthu zakuthupi komanso zimene timamva m'malingaliro athu. Utumiki wake, ndiponso wa atumwi, unali wodzaza ndi machiritso kwa odwala. Yesu pamene anali pamtanda anapereka machiritso a thupi. Kukhulupirira mwa Ambuye kuti apereka machiritso ndi mwai wodabwitsa umene ukanagwirabe ntchito kwa ana a Mulungu kufikira leroli.



I. Uneneri wa Khristu wa machiritso

- A. Yesaya 61:1-2 Yesu anabwera kudzapereka machiritso.
- B. Yesaya 53:3-5 Iye anasenza mavuto ndi zisoni zathu.
- C. Yesaya 35:4-6 Uneneri wa zodabwitsa za Mesiya.

II. Machiritso a Khristu pa dziko lapansi (Uneneri ukwaniritsidwa)

- A. Mateyu 8:16-17 Uneneri wa Yesaya ukwaniritsidwa mwa Khristu.
- B. Mateyu 11:4-5 Anachiritsa akhungu, olumala, akhate, osamva ndi akufa. (Mateyu 15:30-31).
- C. Mateyu 4:23-24 Anachiritsa kudwala ndi matenda a mtundu uliwonse. (Luka 4:40, Luka 7:21).
- D. Machitidwe 10:38 Anachiritsa opsinjika.
- E. Machitidwe 2:22 Mesiya anatsimikiza ntchito zake ndi zodabwitsa, zozizwitsa ndiponso zizindikiro.

III. Mphamvu za machiritso za atumwi

- A. Mateyu 10:1, 7-8 Khristu anapereka mphamvu kwa ophunzira.
- B. Luka 10:1, 9 Ophunzira 70 atumidwa kuti akachiritse odwala.
- C. Marko 16:17-20 Mau anatsimikizika ndi zizindikiro.
- D. Machitidwe 5:12-16 Atumwi anachita zodabwitsa zambiri. (Onaninso: Machitidwe 6:8; 14:8-10; 19:11-12; Machitidwe 28:8)

IV. Mphatso ya machiritso

- A. 1 Akorinto 12:4, 9 Machiritso ndi mphatso.
- B. 1 Akorinto 12:29-31 Onse sikuti ali ndi mphatso imodzi yomweyo.

V. Khristu ali ndi mphamvu zomwezo ngakhale lero

- A. Ahebri 13:8 Yesu Khristu ali yemweyo.
- B. Mateyu 28:18 Khristu ali ndi mphamvu.
- C. Aefeso 3:20-21 Akhoza kuchita koposa m'mene tingamupemphere.

VI. Malangizo kwa odwala (Itanani, dzozani, pempherani)

- A. Yakobo 5:14-16 Akulu a mpingo adzoze odwalayo.
- B. Marko 6:12-13 Ophunzira adzoze odwalayo.
- C. Machitidwe 28:8-9 Kusanjika manja. (Marko 16:18).

VII. Tikuyenera kukhala a chikhulupiriro

- A. Marko 11:22 Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.
- B. Mateyu 13:58 Kusakhulupirira kumaletsa Khristu kuti asagwire ntchito.
- C. Mateyu 17:20-21 Chikhulupiriro chochitachita ndi champhamvu chimabwera ndi kupemphera komanso kusala kudya.

VIII. Kufunikira kwa kufunafuna Mulungu

- A. Masalmo 103:2-3 Machiritso amachokera kwa Mulungu.
- B. 2 Mbiri 16:12 Asa sanafunefune Ambuye.
- C. Mateyu 7:7-11 Pemphani ndipo chidzapatsidwa kwa inu.
- D. 1 Yohane 5:14 Pemphani molingana ndi chifuniro chake.
- E. Ahebri 11:6 Mulungu amapereka mphotho kwa wofunafuna.
- F. 2 Akorinto 12:7-9 Machiritso nthawi zonse sakhala yankho la Mulungu.

IX. Chifundo cha Khristu

- A. Mateyu 14:14 Yesu anagwidwa ndi chifundo.
- B. Marko 1:40-43 Yesu anachiritsa wakhate.
- C. Mateyu 9:35-36 Anthu amafuna mbusa.
- D. Ahebri 4:15-16 Yesu amakhudzidwa ndi kudwala kwathu.

Kumaliza

Ndipo kwa Iye amene angathe kuchita koposaposatatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu ya kuchita mwa ife, kwa Iye ukhale ulemerero mu Mpingo ndi mwa Khristu Yesu, kufikira mibadwo yonse ya nthawi za nthawi. Amen. — Aefeso 3:20-21

Machiritso akumwamba

“Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndi uze anthu osauka Uthenga Wabwino: anandituma Ine kulalikirira am’nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyanso, kutulutsa ndi ufulu ophwanyika.”

Imodzi mwa ndime zosangalatsa m’malemba ikupezeka pa Luka 4:18 pomwe Khristu anawerenga kwa anthu mu sunagoge pa tsiku la sabata. Iye anawerenga ndime yochokera kwa mneneri Yesaya ndipo ananena za cholinga cha maitanidwe ndi utumiki wake. Mfundo yaikulu ndipo imene ikupezeka mwambiri pa utumiki wa Khristu ndiyo



yakuti moyo uchiritsidwe ku gawo la uzimu. Posatengera kena kalikonse kamene tachita, Iye anapereka kwaulere chisomo cha machiritso pa miyoyo ya anthu komanso anabweretsa chiyanjantso pakati pa Mulungu ndi munthu kudzera m’mwazi wake wopepesera machimo. Womangidwa anamasulidwa ku uchimo, iwo amene anali akhungu ku uzimu analandira kuwala, ndipo iwo amene anali kakasi analandira chiyembekezo cha chipulumutso cha moyo.

“Yesu amalamulira pa zonse ndipo mpaka pano akhoza kuchiritsa mtundu uliwonse wa kudwala ndi matenda.”

Yesaya anenera za Khristu

Machiritso odabwitsa a Khristu mwa Mzimu ananedwa mwa ulosi pa Yesaya 53:4-5: “Zoonadi Iye ananyamula zowawa

zathu, ndi kusenza zisoni zathu...Koma Iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natundudwidwa chifukwa cha mphulupulu zathu...ndipo ndi mikwingwirima yake ife tachiritsidwa.” Molingana ndi m’mene zilili masiku ano komanso pofuna kunena momveka bwino, kuchiritsidwa ndi mabala ake kutanthauza zimene Khristu anachita potipatsa machiritso auzimu ndiponso kuombedwa kwa moyo ku mphamvu ya uchimo. Kuphatikiza apo, malemba amanena kuti Yesu anasenza zowawa zathu. Mau akuti “zowawa” tingawatanthauzire kuti “kudwala, matenda, nkhwawa, kuzunzika.” Yesu anakwaniritsa chimenecho komanso maulosi ena amene amaneneratu za machiritso ake athupi odabwitsa pamene maso a akhungu adzaphenyuka komanso makutu awo a osamva adzatsekuka (Yesaya 35:4-6).

Khristu anachiritsa odwala

Nkovuta kwambiri kusiyanyitsa utumiki wa machiritso auzimu a Khristu pamene anali panso ndi utumiki wa machiritso ake a thupi, popeza zonsezi ndi zolumikizana pamodzi. Yesu anauza ophunzira a Yohane Mbatizi kuti apite nakamuuze kuti “akhungu alandira kuona kwao,

ndi opunduka miyendo ayenda, akhate akonzedwa, ndi ogontha akumva, ndi akufa aukitsidwa” (Mateyu 11:4-5). Ndipo pa Mateyu 8:16-17 akutitsimikizira momveka bwino kuti machiritso a Khristu a kuthupi amachitika kuti akwaniritse mauneneri. “[Iye] nachiritsa akudwala onse; kotero kuti chikwaniridwe chonenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti, Iye yekha anatenga zofooka zathu, nanyamula nthenda zathu.” Yesu anachiritsa mitundu yonse ya matenda ndi kudwala konse (Mateyu 4:23-24) ndipo anachiritsa onse amene anali “osautsidwa ndi mdierekezi” (Machitidwe 10:38). Yesu anaonetsedwa kuti anatsimikizidwa komanso anatomizidwa ndi Mulungu kudzera mu zodabwitsa, zozizwitsa, ndiponso zizindikiro zimene anachita pamaso pa anthu (Machitidwe 2:22).

Ophunzira anachiritsa

Yesu anaperekanso mphamvu kwa ophunzira ake “yakuchiza nthenda iliyonse ndi zofooka zonse” (Mateyu 10:1). Ophunzira 70 amene anatomuzidwa kuti akalalikirira uthenga wabwino anawalangiza kuti “chiritsani odwala” (Luka 10:9). Pa Machitidwe 5:12 akutiya kuti, “Ndipo mwa manja a atumwi zizindikiro ndi zozizwa zambiri zinachitidwa pa anthu.” Mau a Mulungu anatsimikizika ndi zizindikiro zimene zinawatsatira atumwi a mpingo oyambawo (Marko 16:17-20).

Mphatso ya machiritso

Mphatso ya machiritso ndi mphatso yakumwamba imene imaperekedwanso ndi Woyera Mzimu ku mpingo (1 Akorinto 12:4-9). Ndi imodzi mwa mphatso zosiyanasiyana zimene Mulungu akhoza kupereka kuti uthenga wabwino upindule molingana ndi m’mene Iye akuonera. Mphatso ya machiritso yoperekedwa pa kusanjikidwa manja siiperekedwa kwa oyera mtima onse. Pa I Akorinto 12:29-30 akufunsa kuti: “Kodi ali onse atumwi? Ali aneneri onse kodi? ...Ali onse ochita zozizwa? Ali nazo mphatso za machiritso onse kodi?” Yankho lake ku mafunso onsewa ndilo “ayi” wamkulu. Si onse amene ali ndi mphatso zofanana, koma Mzimu wa Mulungu amapereka mphatso zimene zili zoyenera kwa munthu kapenanso thupi la okhulupirira pa nthawi yake zoyenera mu nyengo iliyonseyo.

Tikaona mu mbiri pakuoneka chionetsero chachikulu cha machiritso athupi osiyanasiyana mu nthawi ya Kukonzedwanso kwa mpingo, mphamvu yodabwitsa ya Mesiya siinazirale ngakhale mu mbadwo uno. Iye akanali mpulumutsi wa moyo, ndi mchiritso wa thupi komanso

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)



maganizo. Yesu amalamulira pa zonse ndipo mpaka pano akhoza kuchiritsa mtundu uliwonse wa kudwala ndi matenda. “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi kunthawi zonse” (Ahebri 13:8). Yesu anati, “Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi... ndipo onani, Ine ndili pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano” (Mateyu 28:18-20).

Kulowererapo kwakumwamba

Pali chisomo chodabwitsa chimene Mulungu amapereka kwa ana ake m’nthawi ya kudwala komanso kuzunzika. Ngakhale kuti oyera mtima nawonso amatha kudwala komanso kuvutika ndi matenda, iwo akhoza kulandira machiritso athupi kudzera mwa Khristu. Machiritso akumwamba sichinthu chochitika ndi mphamvu yathupi kapena chimene chimachitika mwa mphamvu ya munthu. Kumakhala kulowerera kwa kumwamba pamene Mulungu wasintha za

dziko ndiponso ndi kuchita zimene zinali zosatheka. Kuyang’ana kwa Yesu kuti tilandire machiritso athupi ndi komanso maganizo ndi mwai wa ana a Mulungu ndipo ndi chimodzi mwa cholowa chimene timachipeza potumikira Ambuye. Mulungu wadzitsimikiza yekha kuti ndiye mchiritsi wa ana ake mu nyengo ino.

Malangizo kwa odwala

Baibulo likupereka malangizo kwa odwala mu Yakobo 5:14-16. “Pali wina kodi odwala mwa inu? Adziitanire akulu a Mpingo, ndipo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m’dzina la Ambuye: ndipo pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa; ndipo ngati adachita machimo adzakhululukidwa kwa iye. Chifukwa chake muvomerezane wina ndi mnzake machimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzake kuti muchiritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukulu m’machitidwe ake.”

Odwala akulangizidwa, mwa kufuna kwao komanso chikhulupiriro chao, kuti aitane akulu a mpingo. Akulu a mpingowo akuyenera kutsata chitsanzo cha ophunzira (Marko 6:12-13) ndi kudzoza odwalayo ndi mafuta. Mphamvu siili mu mafutawo koma mu kumvera Mau a Mulungu. Akulu a mpingo akuyenera kutsatira chitsanzo chimene anaonetsa Khristu ndi Atumwi pakusanjika manja pa odwala ndi kupemphera (Marko 16:18, Machitidwe 28:8-9). Pamakhala kupereka kwa mdalitso komanso mphamvu kudzera mu kusanjika manja ndipo Mulungu amalemekeza atumiki ake oyera mtima.

Kufunikira kwa chikhulupiriro

Nthawi zina anthu amachiritsidwa kudzera mu chikhulupiriro cha anzawo ndipo nthawi zina chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Koma chofunikira ndi choyenera ndicho chakuti chikhulupiriro chikhale mwa Mulungu komanso timudalire Iyeyo. Yesu mwini wake, pamene anali ku Nazarete, sanachite zodabwitsa zambiri chifukwa cha kusakhulupirira kwa anthu (Mateyu 13:58). Pamene chikhulupiriro mwa Mulungu chokhala ngati kanjere ka mpiru chikhoza kusuntha mapiri, nkofunika kuzindikira kuti chikhulupiriro chochitachita ndiponso chodabwitsa chimabwera ndi pemphero kapena kusala kudya basi. (Mateyu 17:20-21). Ngakhale kuti zilipo nthawi zina zimene Mulungu amasankha kusachiritsa, chikhulupiriro sichiyenera kutepatepa, popeza chikhulupiriro chili mwa Khristu Mwiniwake, osati mu zimene tilandire m’pemphero lathu.

Mwai wa kukhulupirira

Machiritso enieni amachokera kwa Mulungu “amene amachiritsa nthenda zako zonse” (Salmo 103:3). Malemba amatiphunzitsa kuti tiike chikhulupiriro chathu ndi kudalira mwa Mulungu pa zinthu zonse zimene zimakhudza miyoyo yathu. “Koma wopanda chikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye.” (Ahebri 11:6). Amene akudwala ndiponso kuzunzika, akuyenera kufunafuna Mulungu mwachikhulupiriro komanso ndi chiyembekezo. Mu Chipangano Chakale, Mulungu sanakondwere ndi Asa, amene anali ndi nthenda ya kumapazi ake, chifukwa iye anayang’ana kwa asing’anga ndipo sanafunefune Ambuye (2 Mbiri 16:12). Kupita kwa Mulungu chisamakhale chinthu chimene chili chomaliza, koma tikuyenera kubwera kwa Iye ngati Atate amene amakhumba kupatsa ana mphatso zabwino. Kwa anthu ambiri, chiphunzitsa cha machiritso akumwamba chakhala chinthu chomwe chili chovuta kuchilandira. Nkale lonse, sichinayenera kukhala chipsinjo koma chinthu chabwino kuti ifeyo tidziike kwathunthu m’manja a Mulungu wachikondi. Tipezapo mtendere waukulu tikaika chikhulupiriro chathu kwathunthu mwa Mfulumutsi makamaka panthawi imene pali chikaiko.

Bwerani motsimikizika

Pansi pano, Yesu anatomikira kwa anthu osweka mitima ndiponso kwa iwo amene anali ovutika m’magano ndi odwala m’thupi. Iye anachita izi popeza Iye “nachitira iwo chifundo” (Mateyu 14:14). Khristu Yesu lero naye amatha “kumva chifundo ndi zofooka zathu” (Ahebri 4:15-16). Munthu aliyense amene ali mu mdima wa magano kapena kupweteka kwa thupi akhoza kubwera pa mpando wa chisomo ndi chitsimikizo, ndipo apezapo mphamvu ndi thandizo. Ndi chinthu chabwino komanso chamwai pamene tikhulupirira mwa Mesiya ngati mchiritsi wathu wauzimu, wathupi ndi wa m’magano. ■



Kodi nthawi zonse kudwala kumakhala chotsatira cha chilango cha Mulungu pa uchimo kapena cholakwika chinachake m'moyo wa wina wake? Kodi ndi chochokera kwa Mulungu kapena kwa Mdierekezi?

Kudwala komanso matenda m'dziko lapansi ndi zotsatira za uchimo umene umachitika m'munda wa Edeni. Kudwala ka thupi komanso imfa ndilo gawo limodzi la moyo umene anthu opulumutsidwa zimawachitikira. Nthawi zina oyera mtima amadwala chifukwa cha zochitika m'nyengo kapena mthupi mwao. Ndipotu imfa, mwanjira ina iliyonse imene ingabwere, ndiyo njira yopitira ku moyo wosatha kwa Mulungu

Kodi Mulungu nthawi zonse amachiritsa odwala pamene iwo agwiritsa ntchito chikhulupiriro chao?

Mulungu amafunitsitsa kupulumutsa moyo uliwonse ndipo analonjeza kuti sadzasiya kapena kuleka ana ake; komabe Iye sanalonjeze kuti adzachiritsa nthenda iliyonse yathupi. Pali kugwirizana mu Malemba pakati pa kupempha mwachikhulupiriro, kukhulupirira ndi kugonjera ku chifuniro cha Mulungu.

Paulo anali ndi minga mu thupi lake (yesero kapena chivutiko cha mtundu wina wake) ndipo anapempha Mulungu kuti amuchotsere. Paulo anapemphera kangapo ndithu. Mulungu anamuyankha kuti, "Chisomo changa chikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufooko." Paulo analibe uchimo kapenanso kusowa chikhulupiriro; koma pamene yankho la Mulungu linali "ayi," iye anavomera nati, "Chifukwa chake ndisangalala m'mafooko, m'ziwawa, m'zikakamizo, m'mazunzo, m'zipsinjiko, chifukwa cha Khristu; pakuti pamene ndifooka, pamenepo ndili wamphamvu" (2 Akorinto 12:7-10).

Tikuyenera kupemphera molingana ndi chifuniro cha Mulungu mwa chikhulupiriro, kukhulupirira mwa mphamvu yake. Pempherani moyembekezera komanso ndi mzimu wodzichepetsa. Pamene Mulungu wapereka yankho, tikuyenera kulilandira mwa chikhulupiriro ndi kulimbika mtima podziwa kuti chisomo chake chigwira ntchito mokwanira kaya pali machiritso kapena mu kudwala.

Satana akhoza kubweretsa masautso monga anachitira ndi Yobu, komabe chilichonse chimene chingakhudze miyoyo yathu chimayenera kuti chiyambe chavomeredwa ndi Mulungu. Komanso ndi zoonza ndithu kuti Mulungu akhoza kubweretsa kapena kuloleza matenda kuti afike pa matupi athu. Kodi si nthawi ngati izi zamasautso pamene timasendera chifupi ndi Mulungu? Ngakhale m'amasautso tikhoza kudzipereka tokha mopanda mantha kuti Iye atisamalire, makamaka pozindikira kuti adzachita zimene zili zabwino koposa.

Pa Yohane 9:1-11, Yesu anachiritsa munthu amene anabadwa wosaona. Ophunzira ake anayankha, "Ndipo ophunzira ake anamfunsa Iye, nanena, Rabi, anachimwa ndani, ameneyo, kapena atate wake ndi amake, kuti anabadwa wosaona? Yesu anayankha, Sanachimwe ameneyo, kapena atate wake ndi amake; koma kuti ntchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye."

Nthawi zambiri Mulungu amafuna kugwira ntchito yabwino kudzera mwa odwala osati chifukwa cha iye yekha komanso chifukwa cha ena. Pa 2 Akorinto 4:15-17 akuyankha funsoli momveka: "Pakuti zonsezi nza kwa inu, kuti chisomocho, chochulukitsidwa mwa unyinjwo, chichulukitsire chiyamiko ku ulemerero wa Mulungu. Chifukwa chake sitifooka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja uvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti chisautso chathu chopepuka cha kanthawi chitichitira ife kulemera koposa kwakukulu ndi kosatha kwa ulemerero."

Kodi "kukhulupirira Ambuye" ndiye kuti kusiya kulandira thandizo la chipatala?

Malemba amatipunzitsa kuti machiritso ndi chinthu chabwino komanso mdalitso wa Mulungu kwa ana ake. Amaphunzitsanso kuti ngati tikufuna kukondweretsa Mulungu tikuyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Anthu ambiri amanena kuti chikhulupiriro ndi chokhacho chimene chingabweretse machiritso athupi. Kumeneku ndi kulakwitsa Malemba. Chikhulupiriro chimafikira ku gawo lililonse la moyo ndipo kwambiri chimakamba za ubale wathu ndi Mulungu kusiyana ndi zimene wina amachita kapena wachita zokhudza zachipatala.

Pa Aroma 14:22-23 akunena kuti, "Chikhulupiriro chimene uli nacho, ukhale nacho kwa iwe wekha pamaso pa Mulungu. Wodala ndiye amene sadziweruza mwini yekha m'zinthu zomwe iye wazivomereza. Koma iye amene akayikakayika pakudya, atsutsika, chifukwa akudya wopanda chikhulupiriro; ndipo chinthu chilichonse chosatuluka m'chikhulupiriro, ndicho uchimo."

Pali madera ena amene Baibulo silinena zinthu zonse zofunikira ndipo ifeyo timalakwitsa pamene tiikamo zinthu zina motsaliramo. Pali kusiyana ndithu kwa chikhulupiriro pakati pathu ndipo zimenezi zikutanthauza kuti Mulungu akhoza kutitakasa ndi kutitsogolera anthufe mosiyanasiyana malinga ndi m'mene zinthu zachitikira. Pamene oyera mitima akhoza kugwiritsa ntchito dokotala komanso kwinaku akukhulupirira, zilipo nthawi zimene chikhulupiriro chamunthu ndiponso m'mene munthuyo amadzionera zimamupangitsa kuti akane thandizo lakuchipatala. Kukana thandizo lachipatala pamene tadwala kusachitike chifukwa takakamizidwa ndi anzathu koma zikhale zimene tatsimikiza mwachikhulupiriro mu mtima mwathu.

Nkoyenera ndithu kuti ifeyo tiike chikhulupiriro chathu ndi kudalira mwa Ambuye. Funafunani Mulungu ndipo mugonjere kuchifuniro chake ndi cholinga chake kaya mukusautsika ndi matenda kapena muli wathanzi bwinobwino. "Ambuye, kulitsani chikhulupiriro chathu!"



KODI MUKUDZIWA?

Kapena simudziwa kuti thupi lanu lili Kachisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu? ... chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu. —1 Akorinto 6:19-20

Madyedwe osakhala bwino ndi amene akukolezera ku imfa za anthu 678,000 chaka chilichonse ku Amerika. Izi zikuchitika chifukwa cha matenda amene amabwera chifukwa cha kusadya zamagulu komanso kunenepa kwambiri. Mu zaka 30 zapitazi,

mulingo wa anthu onenepa koposera muyezo wachuluka koposa kawiri mwa akulu, koposa katatu mwa ana, ndipo koposa kanai mwa achinyamata (cspinet.org).

Mwana wa Mulungu akuyenera kuzindikira kuti thupi lake ndi kachisi wa Mulungu ndipo akuyenera kulisamalira molingana ndi malangizo abwino a zaumoyo pokudya zakudya zabwino zamagulu komanso kupanga zinthu zolimbitsa thupi.



**Mau a
Nyengo
Yake**

M'DZINA LA YESU

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Koma Petro anati, Siliva ndi golide ndilibe; koma chimene ndili nacho, ichi ndikupatsa, M'dzina la Yesu Khristu Mnazarayo, yenda. —Machitidwe 3:6

Pamene munthu wopunduka chibadwire anali pa chipata cha kachisi kuyang'anitsitsa Petro ndi Yohane kuyembekeza kuti alandira thandizo la ndalama, iwo anamumiritsa iye m'dzina la Yesu, ndipo munthuyo anachiritsidwa ndi mphamvu ya kumwamba. Anthu anadabwa ndipo Petro anawadziwitsa iwo kuti munthuyo sanachiritsidwe mwa mphamvu zao kapena chiyero chao. "Ndipo pa chikhulupiriro cha m'dzina lake dzina lakelo linalimbikitsa iye amene mumuona." Machiritso anabwera mwa chikhulupiriro kudzera m'dzina la Yesu.

Lerolo mphamvu zilipo m'dzina lamphamvu, lodabwitsa ndi lopambana la Yesu. Nthawi zambiri, timatsiriza pemphero lathu ndi mau akuti: "M'dzina la Yesu." Kumeneko ndiko kumaliza kwabwino kwa pemphero, koma mphamvu mu dzina la Yesu ndiye pamtima ndiponso paphata pa kufunafuna Mulungu kuti alowererepo, osati mapeto ake chabe. Palibenso dzina lina limene linaperekedwa pansu pa thambo kusiyana ndi dzina la Yesu. Pamene tiitanira pa dzina la Yesu, ifeyo tikuitana pa dzina la Iye amene ali mlengi wa dziko lapansi, mutu wa mpingo, Mfumu ya mafumu, Mbuye wa Ambuye, alefa ndi omega, woyamba ndi wotsiriza.



CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Satana amadana ndi dzina la Yesu ndipo iye amanjenjemera pa dzinalo. Mizimu yoipa imayenera kuthawa pamene anthu oyera aitanira pa dzina lamphamvulo. Tikhoza kukumana molimba mtima ndi mphamvu za mdima, masautso a moyo uno molimbika, ndipo mdima wa dziko lapansi ndi chiyembekezo, popeza tikhoza kumufikira Iye amene anagonjetsa adani ake onse, kuphatikizapo imfa. Pokhala atumiki ndi ogwira ntchito ya uthenga wabwino, tikuyenera kuti tisaope kuti mwina tilephera kapena sitiphulapo kanthu. Mphamvu za machiritso kapena chisomo cha kutsunga sichathu koma cha Mulungu. Tiyeni tisiye zonse m'manja mwa Mulungu.

Yesu ndiye woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiriro chathu. Tilole chikhulupiriro chathu ndi chiyembekezo chathu chilimbikitsidwe pamene tapempherera miyoyo imene yamangidwa komanso yazikika mu uchimo. Tikhoza kupemphera ndi ulamuliro komanso molimbika mtima pamene tipemphera m'dzina la Yesu. Pamene odwala ndi wosautsika akufunitsitsa kuti apeze thandizo, tikhoza kufunafuna Mulungu motsimikizika kudzera mwa mwana wake wokondeka. Ifetu ndife anthu ndiponso ofooka, koma popeza tili ana a Mulungu, tili ndi mphamvu m'dzina la Yesu. ■